# UNDUNA WA ZACHILENGEDWE NDI KUSINTHA KWA NYENGO

## NTHAMBI YOONA ZA NYENGO NDI KUSINTHA KWA NYENGO


## ULOSI WA KAGWEDWE KA MVULA M'BOMA LA THYOLO M'DZINJA LA 2025-2026

## DZINJA LA 2025/2026 MWACHIDULE

Katenthedwe ka Nyanja ya mchere ya Pacific sikakhudza kwambiri nyengo ya dzinja ya 2025/26.


Boma la Thyolo likuyembekezereka kulandira mvula ya mlingo wokhazikika mu nyengo ya mvula ya 2025/2026.

## October 2025




Madera ambiri kudzakhala otentha ndi opanda mvula mu mweziwu.
Komabe pali kuthekera kwa mvula ya Chizimalupsya yomwe idzabwere ndi mphepo ya mkuntho m'madera ena.


## November 2025




Tiyembekezere mvula ya mlingo ochepera okhazikika mu mweziwu.
Madera ambiri akhoza kudzalandira Mvula ya mlingo wa pakati pa 50mm ndi 100mm yomwe idzakhale ya mabingu ndi ya mphepo ya mkuntho.


Mvula yokhazikika ikuyembekezereka kuyambira sabata lachinayi la mwezi wa November 2025.

## December 2025





Mu December, madera ambiri ali ndikuthekera kolandira mvula ya mlingo okhadzikika kapena kuposera apo wa pakati pa 200mm ndi 250mm. Madera ochepa a kwa TA Nchilamwela, SC Kwethemule ndi TA Changata akuyembekezereka kulandira mvula ya mlingo okwana 300mm

## January 2026





Mwezi wa January ukuyembekezereka kukhala wa chinyontho kwambiri.
Madera ambiri ali ndi kuthekera kolandira mvula ya mlingo okwana 300mm ndi ena ochepa kulandira mvula ya mlingo oposera 300mm monga ngat m'dera la TA Nchilamwela ndi SC Kwethemule.
Ng'amba yosapyola sabata limodzi ikuyembekezereka mu mweziwu.

## February 2026





Mlingo wa mvula okhazikika ikuyembekezeleka m'madera ambiri komanso mvula ya mlingo ochepera okhazikika m'madera ena mu mweziwu.
Mvula ya mlingo wa pakati pa 150mm ndi 200mm ikuyembekezereka madera ambiri.
Pali chiopsezo cha ng'amba yosapyola sabata mu mweziwu.

## March 2026




Mu March, mvula ya mlingo okhazikika wa 150mm ikuyembekezereka m'madera ambiri.
Mvula ya mlingo ochulukirapo wa 200m ikuyembekezereka m'madera ochepa monga ngati kwa SC Kwethemule ndi TA Changata

## April 2025





Mu mweziwu, madera ambiri ali ndi kuthekera kolandira mvula ya mlingo okhazikika kapena kuchepera apo.
Mvula ya mlingo wa pakati pa 100mm ndi 150mm ikuyembekezereka m'madera ambiri.

Nyengo ya mvula ikuyembekezereka kufika kumapeto sabata lachiwiri la mwezi wa April 2026.

Mvula yokhazikika ikuyembekezereka sabata lachinayi ya mwezi wa November, 2025.
Nyengo ya mvula ikuyembekezereka kufika kumapeto sabata lachiwiri la mwezi wa April 2026.
Nyengo ya dzinja ikuyembekezereka kukhala yotali masiku a pakati pa 130 ndi 140.
Pali chiopsezo chachikulu cha ng'amba ya masiku pafupifupi sabata imodzi mu mwezi wa January, ndi mwezi wa February.

| THYOLO | | | |
|---|---|---|---|
| MONTH | NORMAL RANGE | | FORECAST |
| OCT | 9.8 | 44.6 | 25.5 |
| NOV | 66.6 | 123.2 | 47.4 |
| DEC | 182.7 | 319.5 | 293.1 |
| JAN | 270.9 | 432.1 | 327.0 |
| FEB | 163.6 | 252.1 | 145.8 |
| MAR | 127.6 | 199.3 | 174.9 |
| APR | 10.8 | 59.2 | 60.9 |




**Ulosiwu udzasindikizidwanso mu mwezi wa December 2025**

Zasindikizidwa ndi thandizo lochokera ku:


**Mukafuna kudziwa zambiri lemberani kwa:**
The Director of Climate Change and Meteorological Services, P.O. Box 1808,Blantyre.
Tel +265 1 82 47 12 / Cell: +265 882 26 65 79 Email: metdept@metmalawi.gov.mw ; Website: www.metmalawi.gov.mw